COVID-19: Nthawi zonse satilani uphungu wa boma komanso acitetezo za umoyo.

DIGNITY

Umoyo

Nkhani 7

hello@dignityonline.org.uk
+447340 573 937

Kukhala Nacho Chikhulupililo Pamodzi

Nichapa fupi kumva nkhani za Baibulo kapena ku anthu omwe atsatila Yesu leelo ndi kulingalila, “Sini nakakwanitsa kuchita kalikonse motere.”

Ahebri 11:1 ndi 6 ikuti, “Sopano chikhulupililo ndi chidwi mwazomwe tiyembekezera ndi kukhutila mwazomwe sitioon...Ndipo kopanda chikhulupililo sichapafupi kukondweletsa Mulungu, chifukwa yense akudza kwa iye afunika ku khulupilila kuti alipo ndipo apatsa mphoto kwa awo omusakila mwachoonadi iye.”

Ahebri 11 amasula chimodzi mwa zofunikila zoyenga po tumikila Mulungu zofunika niche ‘khulupililo.’ Pakati pazina ndikulankhula za Nowa ndi Abrahamu, Ayunda awiri ‘opambana’ anasatila Mulungu. Nkhani zawo zili mu chipangano chakale.

Tipeza nkhani ya Nowa mu Genesis 6 komwe ikuti, “Nowa anachita zonse momwe Mulungu anamuuzila.” Mulungu anakatuma madzi ndipo anafuna kuteteza awo omukhulupilila iye. Anapempha Nowa kuti amange choombo komwe kunalibe madzi! Lingalilani izi! Anthu nikumseka Nowa nalingalila ali wokonya. Madzi akudza ndipo aliyese kuchosako Nowa ndi banja lache anaphedwa. Chikhulupililo cha Nowa mwa Mulungu china mupulumutsa.

Abrahamu ndi wosiyanako kwambili (Genesis 12-25). Abrahamu anauzidwa ndi Mulungu kuti azakhala ndi mwana wamuna ngakhale kuti anali wamukulu ndi Sarah sakanakhala ndi mwana. Sarah sana khulupilile izi iyayi. Anaseka pomwe Abrahamu ana muuza. Mulungu anauza Abrahamu kuti azukulu ace azachuluka monga nyenyezi. Abrahamu anabvutika kukhulupilila. Pamapeto, ngakhale mumabvutowo, Mulungu anapasa Abrahamu ndi Sarah mwana ndikuzazikitsa lonjezo yache kwa iwo. Ahebri 11 ikuti mwa chikhulupililo Abrahamu ndi Sarah ana khala ni mwana!

Chikhulupililo chipimidwa mu zochita – chioneka momwe tikhalila. Kutanthauza kuti tichita zomwe Mulungu afuna ife ku chita, ngakhale kuti sitimvetsetsa chifukwa! Ngati Mulungu wakamba kuti azatipasa ndi kutiteteza tikhulupilile izi ndi malingalilo amodzi polaka mantha. Chikhulupililo ndi kuika ku dalila yathu mwa Mululngu ndi mphanvu zache mukucita nchito mukhalidwe kupambana kukwanitsa kwathu. Pomwe tasankha kuika chikhulupililo mwa Mulungu tisankha ku dalila mwa Mulungu mwini, mau ace (Baibulo), ndi zochita zache ndi zikwi za anthu. Mulungu akwanitsa kuchita moposa tipemphera kapena kulingalila.

Ziyikeni mu Zocita!

Kodi Mulungu afuna kuti muchite chiani? Mwezi watha tinayangana pakuyamba Bungwe Lamoyo. Kodi tifuna kuika chikhulupililo chathu po yamba? Kuziika tokha ‘pa bwalo’ pagulu? Kodi Mulungu ati funsa ife kumasula Yesu ku anthu kapena kupeza ndalama kuthandiza wina? Kopanda chikhulupililo sizotheka kukhulupilila Mulungu. Dalila. Chita. Oona zomwe Mulungu achita!

Pephelani kuti:

1) Mulungu azakupasa chikhulupililo cha chikulu ndi kukuonetsa mogwiritsila nchito (Aefenso 2:8-10)
2) Kukaiyika kulikonse ndi mantha zizasila pomwe uku belenga Baibulo ndi kuchela ku liwu la Mulungu pa umoyo wako.

Bernard anapemphera ndi Peter *omwe anali osweka mtima pambuyo potaikidwa mkazi wache. “Pomwe tinali kupemphera ndi namva chinthu cina monga chimphepo champhamvu...Koma kunalibe mphepo inali kuomba, koma ndinamva mphepo yaikulu ili kuomba. Pambuyo pache ndi nayamba kumva ku masuka monga ndi nali mu ukapolo koma sopano ndine omasuka”

- Bernard ndi Peter*, Kalweo, Zambia



Phunziloyi iku sisimusidwa ndi “Chikulupililo - Tiyenela Kukhulupilila” phunzilo mu mu Kondani Mudzi Wanu, buku yomwe ikuthandizila kutumikila ena ndi uthenga wa Yesu. Mungathe kupeze zambiri pa: **dignityonline.org.uk/publications**

Dignity ndi bungwe ya zaulele yosindikizidwa pa No. 1122656. Dignity (Worldwide) ndi kampani yoziyimilila pa yokha, yosindikizidwa ku England ndi Walesi No. 6394480. Dignity Zambia Limited ndi kampani yomwe anthu aphindulako yosindikizidwa mu ziko la Zambia pa No. 117117

*dzina lisinthidwa ku lamwine

Chewa